

(1)
GALILEYA
(1)
Mtsinje wa Yorodano
(2) SAMARIYA
(2)
(4) PEREYA
(4)
(3) YUDEYA
(3)
Kuchokera ku AFRIKA

SABATA LACHIŴIRI: UKHANDA WA KHRISTU
TSIKU LACHISANU: MALO AMENE YESU ANAKHALA NDI KUPHUNZITSA

1. Limeneli ndi phunziro lotsiriza mu Sabata Lachiŵiri. M'masabata aŵiriŵa takhala tikuphunzira za Khristu asanabadwe. Taonanso zimene zinachitika pa kubadwa kwake. Taphunzira za kumvera kwake kwa Mulungu ndi makolo ake. Dzulo tinaphunzira ntchito ya Yohane Mbatizi.

Iye asanaŵabatize iwo, kodi Yohane Mbatizi anauza anthu kuchita chiyani kuti akunzekere Khristu?

______________________________

Kodi ndi umboni wa chitsanzo chotani umene Yohane Mbatizi amatiphunzitsa mmene tingakhalire?

______________________________

==========================================================================

2. Yohane anauza anthu kuti alape mmalo mofuna kukonzekera Khristu. Chitsanzo chake chimatiphunzitsa ife kukhala mboni za Khristu zokhulupirika.

Lero tiona za dziko limene Yesu anakhala ndi kuphunzitsa. Yesu anali kukhala m'dziko la Israyeli. Dziko limeneli limatchedwanso kuti Palestina. Ndi dziko laling'ono. Siriri kutali ndi Afrika. Magalimoto, sitima za m'madzi ndi ndege zikhoza kupita kuchokera ku Afrika kupita ku Israyeli. Lero tiphunzira kulemba zigawo zinayi za Israyeli pa mapu. Zigawo zake ndi izi:

(1) Galileya
(2) Samaliya
(3) Yudeya
(4) Pereya

Kodi ndi kotheka kuti munthu akhoza kuchoka kuno ku Afrika kupita ku Israyeli?

______________________________

==========================================================================

3. Chaka ndi chaka anthu ambiri amapita kuchokera kuno ku Afrika kupita ku Israyeli. Pamene Yesu anali kukhala mu Israyeli dziko limagaŵidwa mzigawo zinayi. Zigawo zimenezi zinali kutchedwa m'madera. Ife tikhoza kuphunzira zigawo kapena madera ameneŵa mosavuta kuchokera pa Mapu ndi mtundu wa chithunzi cha dziko. Mapu amatithandiza ife kuona kuti dziko ndi lotani. Mudzaonetsetsa kuti mukauzidwa kuyang'ana pa mapu nthaŵi

iliyonse muzichitadi.

Tsopano onani mapu amene ali pafupi ndi tsamba lino. Tawerengani zigawo kapena m'madera.

Kodi alipo angati? ____________________

==========================================================================


4. Kunali madera anayi a Israyeli pa nthaŵi ya Khristu. Maina a zigawo zimenezi alembedwa pa mapupo. Iwo ndi (1) Galileya, (2) Samariya, (3) Yudeya, ndi (4) Pereya.

Pansi pa dzina lililonse pali mzere. Tiri kufuna kuti inu mulembenso dzina lililonse pansi pa mzerewo. Chimenechi chidzakuthandizani kuti muphunzire mainawo. Chidzakuthandizaninso kuphunzira kumene kuli dera lililonse.

Tsopano pitaninso pa mapu ndikulemba dzina lililonse pansi pake.

==========================================================================

Dziko la Israel m'nthaŵi ya Khristu



5. Mizere yonse imene ili ndi manambala iyenera kukhala yodzaza. Ife tikufuna kuphunzira maina a m'madera ameneŵa. Ndi malo ofunika koposa kwa anthu amene amaphunzira Buku Lopatulika. Ndi malo amene Yesu amakhalako ndi kuphunzitsa.

Kodi inu mukuganiza kuti chikuthandizani mukaphunzira malo ameneŵa?

______________________

Ngati mwalemba "Inde nenani mmene muli kuganizira kuti chidzakuthandizani?

______________________________________________________________

______________________________________________________________

=====================================================================

6. Tidzakambirana za zimenezi tonse pamodzi. Ngati mutadziŵa zigawo za Israeli, chidzakuthandizani kudziŵa komwe Yesu anapita. Chidzakuthandizaninso kudziŵa zomwe anachita. Mapu akhoza kutithandiza ife. Akhoza kutionetsa kumene malo ali. Mapu amationetsanso ife ngati malo ena ali cha kumpoto kapena ku mmwera kwa malo ena. Amationetsanso ngati malo ena ali cha kummaŵa kapena cha kumadzulo kwa malo ena.

Kodi mapuŵa amachita zimenezi motani? Njira yake nayi: malo amene ali pamwamba pa malo ena pa mapupo ndi cha kumpoto kwa malo amenewo. Pa mapu aŵa Samariya ali pamwamba pa Yudeya. Onani pa mapupo kuti muone zimenezi. Izi ziri kuonetsa kuti ku Israeli Samariya ali cha kumpoto kwa Yudeya.

Taonani Samariya pamapupo. Kodi ndi dera liti limene lili chakumpoto (kapena pamwamba) kwa Samariya?

____________________________________

=====================================================================

7. Galileya ndiye ali pamwamba pa Samariya. Chifukwa cha ichi, Galileya ali kumpoto kwa Samariya. Malo alionse pamapu amene ali pansi pa malo ena ndi kummwera kwa malowo. Samariya ali pansi pa Galileya pa mapu ameneŵa. Taonani pamapu. Izi zikutionetsa kuti Samariya ali kum'mwera kwa Galileya.

Onaninso pamapu kachiŵiri. Kodi ndi dera liti lili kum'mwera kwa (kapena pansi pa) Samariya?

________________________________________


8. Yudeya ali pansi pa Samariya. Zimenezi zimaonetsa kuti ali kummwera kwa Samariya. Malo alionse pamapu amene ali chakumanja kwa malo ena ndi kummaŵa kwa malo enawo. Pamapu aŵa, mtsinje wa Yordano uli chaku dzanja lamanja kwa Samariya. Taonani pamapupo. Izi zimaonetsa kuti mtsinje wa Yordano uli cha kudzanja lamanja kwa Samariya.

Taonaninso pamapupo. Kodi ndi dera liti lili cha kummaŵa (kapena ku dzanja lamanja) kwa Samariya?

________________________________

==========================================================================

Dziko la Israeli m'nthaŵi ya Khristu



9. Dera la cha kummaŵa kwa Samariya ndi Pereya. Mtsinje wa Yordano ulinso cha kummaŵa kwa Samariya. Koma dera la ku mmaŵalo ndi Pereya.
Malo aliwonse pamapu amene ali kudzanja lamanzere kwa malo ena a amenewo. Pamapu aŵa, Samariya ali chakumanzere kwa mtsinje wa Yordano Taonani pamapu. Izi zili kuonetsa kuti Samariya ali cha kumadzulo kwa mtsinje wa Yordano.

Yang'ananinso pamapu. Pezani nyanja ya Galileya. Kodi ndi dera liti limene lili (kapena dzanja la manzere) cha kunyanja ya Galileya?

______________________________

=====================================================================

10. Dera la Galileya ndilo lili chakumadzulo kwa nyanja ya Galileya. Kumbukirani pamapu kuti kumwamba ndi kumpoto. Pansi ndi kummwera. Chakumanja ndi kummaŵa. Cha kumanzere ndi kumadzulo.
Dera limene Yesu anayamba kulalikira ndi la Galileya. Limeneli ndi dera la kumpoto. Yesu anakulira mu mzinda wotchedwa Nazarete. Nazarete anali m'dera la Galileya. Koma kaŵirikaŵiri Yesu anali kupita kudera la Yudeya.

Yang'anani pamapu. Ngati Yesu anali m'Galileya ndi kupita moluniika cha kummwera kwa Yudeya, kodi ndi dera liti limene poyamba Iye anayenera kudzeramo?

__________________________________________________________

=====================================================================

11. Iye anayenera kupyola Samariya. Dera limeneli linali pakati pa Yudeya ndi Galileya. Anthu a mu Samariya sanali Ayuda. Iwo anali kutchedwa Asamariya. Ayuda sanali kukonda Asamariya. Nthaŵi zambiri Ayuda amene anali kupita kuchokera ku Galileya kupita ku Yudeya anali kukana kudzera popyola m'Samariya. Iwo anali kudzera njira ina. Koma Yesu anachezera Samariya. Iye analankhulana ndi mkazi pa chitsime. Asamariya ambiri analandira Yesu.

Tayang'ananinso mapuwo. Tiyeni tinene kuti mu Yuda waku Galileya, ali kufuna kupita ku Yudeya, koma sakufuna kudzera mopyola m'Samariya. Kotero iye aoloka mtsinje wa Yordano. Iye apita modutsa dera la cha kummaŵa kwa tsidya la Yordano. Kodi dera limeneli ndi liti?

__________________________________

=====================================================================


12. Dera la cha kummaŵa kwa mtsinje wa Yordano ndi Pereya. Silinatchulidwe ndi dzina limeneli m'Buku Lopatulika. Limangotchulidwa kuti ku tsidya kwa Yordani. Nthaŵi zina pamene Yesu anali kupita ku Yudeya pochokera ku Galileya, Iye anali kudzera podutsa ku Pereya. Kumaoneka kuti Yesu anabatizidwira m'dera limeneli. Iye analalikiranso kumeneko.

Tayang'anani pamapu. Kodi ndi dera liti limene lili cha kum'mwera kwa Samariya?

______________________________

==========================================================

Dziko la Israeli m'nthaŵi ya Khristu



13. Dera la kummwera ndi Yudeya. Yesu anali kukhala m'Galileya, koma sanali kupita kaŵirikaŵiri ku Yudeya. Iye anabadwira ku Betelehemu wa Yudeya. Iye anali kupita ku phwando la Paskha ku Yerusalemu. Kumeneku kunalinso ku Yudeya. Patapita nthaŵi Yesu anapachikidwa ku Yudeya kunja kwa mzinda wa Yerusalemu.

Kaŵirikaŵiri Yesu anali kumapita ku Yudeya, koma mudzi wake unali kutali ku dera la kumpoto. Pa mapu olingana ndi tsamba ili lembani dzina la dera la kumpoto.

==========================================================================

14. Taonani ngati mwalemba Galileya pa nzere woyambawo. Pamene Yesu anali kupita modutsa cha kummwera, Iye anali kudzera dera limene Ayuda sanali kukhala. Iye analalikira kwa a Samariya. Ndipo Iye anali kupitirira kuloŵa mu Yudeya.

Pa mapupa lembani dzina la dera la cha kummwera kwa Galileya limene Yesu anapyolamo.

==========================================================================

15. Onani ngati mwalemba Samariya pa mnzere wachiŵiriwo. Kuchokera ku Samariya kaŵirikaŵiri Yesu anali kupita ku Yerusalemu. Kachisi anali kumeneko. Yesu anali kulalikira m'Kachisi. Iye anachita zozizwitsa ndi kuphunzitsa ophunzira ake.


Pamapupo, lembani dzina la dera la chakummwera komwe Yerusalemu ali.

==========================================================================

16. Munayenera kulemba kuti Yudeya pa mzere wachitatuwo. Pamene Yesu anali kubwerera ku Galileya nthaŵi zina anali kudzera popyola Samariya. Koma nthaŵi zina Iye anali kumadzera ku Pereya. Iye anali kuoloka mtsinje wa Yordani. Ndipo Iye anali kupyola m'dera la chakummaŵa. Iye anali kulalikira kwa Ayuda a m'dera limeneli pamene Iye anali kubwerera ku Galileya.

Pamapupo, lembani dzina la dera la cha kummaŵa limene nthaŵi zina Yesu anali kulalikirako.

==========================================================================


(1)
Nazareti
Nyanja ya Galileya
Mtsinje wa Yorodano
(2)
(4)
(3)
Yerusalemu
Betelehemu
Nyanja ya mchere
Kuchokera ku AFRIKA

17. Munayenera kulemba Pereya pa mzere wachinayi. Mwaphunzira maina ndi malo a madera anayi. Iwo ndi Galileya, Samariya, Yudeya, ndi Pereya Malo ameneŵa ndi kumene Yesu anakhalako ndi kuphunzitsa. Ndi ofunika kwambiri kwa ife.

Kodi masiku ano ndi kutheka kuchezera dziko la Yesu? ______________


==================================================================

18. Ndi kotheka ndithu kuchezera dziko limeneli masiku ano. Mwina inu muli kudziŵa za wina wake amene anapitako kale kumeneko.

Tsopano yang'anani mapu omwe ayang'anana ndi tsambali m'dera lililonse muli mzere. Pamapupo lembani dzina la dera lililonse la Aisraeli pa mzerepo.

==================================================================

Dziko la Israel m'nthaŵi ya Khristu



SABATA LACHITATU: KHRISTU AKONZEKERA NTCHITO YAKE
TSIKU LOYAMBA: YESU ANABATIZIDWA KUTI ACHITE CHIFUNIRO CHA MULUNGU

1. Mwalandiridwa ku sabata latsopano lamaphunziro a za Yesu. Sabata lapita munaphunzira zigawo za Israeli kumene Yesu anakhala ndi kuphunzitsa.

Lembani maina a zigawo za mapu omwe ali pafupi ndi tsambali.

==========================================================================

2. Maderaŵa ndi (1) Galileya, (2) Samariya, (3) Yudeya, (4) Pereya. Malo ameneŵa ndi ofunika kwa ife chifukwa ndiko kumene Yesu anagwirako ntchito.

Kodi Khristu anakonzekera kugwira bwanji ntchito yake? Chimenechi ndi chimene tidzaphunzira sabata ino. Tiyamba ndi ubatizo wa Yesu. Ndipo tiphunzira zinthu ziŵiri za ubatizo.

(1) Cholinga ndi kubatizidwa kwa Yesu kunali kosiyana ndi kwathu chifukwa Iye analibe tchimo.

(2) Yesu anabatizidwa kuti achite chifuniro chonse cha Mulungu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 3:13-15. Kodi ndani anabatiza Yesu?

________________________________________

==========================================================================

3. Yohane Mbatizi ndiye amene anachita zimenezi. Kumbukirani kuti iye anali kukonzera Khristu njira. Iye anali kulalikira kuti anthu alape machimo. Iye anali kubatiza anthu amene analapa.

Kodi inu mukukumbukira nthaŵi imene munali walitsiro ndi wotopa? Mwina munali kulima tsiku lonse lathunthu. Mwina mwakhala tsiku lathunthu muli kuyenda paulendo ndipo mumapita kunyumba ndi kusamba.

Kodi inu munamva bwanji mutatha kusamba? ____________________________

________________________________________________________________

==========================================================================

4. Muyenera kumva bwino, komanso wotopa pang'ono. Mwina inu mumakhala wokondwa. M'njira ina ubatizo umakhala ngati kusamba. Pamene ife tikusamba matupi athu, madzi amachotsa litsiro ndipo timakhala audongo.

Ubatizo umaonetsa kuti machimo athu achotsedwa ndipo tsopano ndife aukhondo. Koma madzi aubatizo satsuka machimo athu. Tchimo limakhala mkati mwa ife. Limakhala m'maganizo ndi m'miyoyo yathu. Ndi Mulungu yekha amene angachotse tchimo mwa ife. Iye amachita zimenezi pamene takhulupirira Khristu ndi kufulatira tchimo.

Kodi tiyenera kuchita chiyani ndi tchimo tisanabatizidwe? ____________

________________________________

==========================================================================

5. Ife tiyenera kutembenuka kumachimo. Ife tiyenera kukhulupirira Khristu. Ngati tichita zimenezi Mulungu amachotsa tchimo m'miyoyo yathu. Koma sitingathe kuona Mulungu akuchita zimenezi. Koma Mulungu anatipatsa chithunzi. Chithunzichi ndi ubatizo. Madzi aubatizo amatsuka kunja kwa matupi athu. Izi zimasonyeza zomwe Mulungu amachita mkati mwa munthu wotembenuka mtima.

Yohane Mbatizi anali kulalikira pafupi ndi mtsinje wa Yordani. Anthu ambiri anali kubwera kudzamva iye ali kulankhula ndi kuwauza kuti alape. Pamene iwo analapa, iye anaŵabatiza.

Mateyu 3:6,13:

> Nabatizidwa ndi iye mu mtsinje wa Yordani, alikuulula machimo awo ... Pamenepo Yesu anachokera ku Galileya nadza ku Yordani kwa Yohane, kudzabatizidwa ndi iye.

Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anadza kwa Yohane pa nthaŵi imeneyi?

____________________________________________________________________

==========================================================================

6. Yesu anabwera kudzabatizidwa ndi Yohane. Koma Yohane sanafune kubatiza Yesu. Iye anadziganizira kuti sanali woyenera kuchita zimenezi. Yohane anafuna kuti abatize Yesu.

Kodi ubatizo wa Yohane unali kuonetsa kuti munthu wachita chiyani?

____________________________________________________________________

==========================================================================

7. Izi zimasonyeza kuti munthu walapadi kapena kutembenuka kuchoka ku machimo ake. Kwa Yohane chinaoneka kuti sichinali cholondola kuti Yohane abatize Yesu. Yesu sanachimwe konse.

Kodi Yesu anafunika kufulatira tchimo? ____________________

==========================================================================

8. Yesu sanayenere kutembenuka mtima. Yesu sanabatizidwe chifukwa chakuti anachimwa ayi. Iye sanali wofanana ndi ife m'njira imeneyi.

Ahebri 4:15:

> Pakuti sitiri naye mkulu wa ansembe wosatha kumva chifundo ndi zofooka zathu; koma woyesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda uchimo.

Ndimeyi ikunena za Yesu. Yesu anayesedwa m'njira zambiri monga momwe ife timayesedwera.

Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu sanafunike kutembenuka mtima?

______________________________________________________

==========================================================================

9. Yesu sanachite tchimo lililonse. Ubatizo wathu umaonetsa kuti ife ndife ochimwa. Ife timabatizidwa pamene tifulatira machimo athu. Koma Yesu sanayenere kutembenuka mtima kuchokera ku machimo ake. Iye sanachimwe konse.

Kodi Yesu anabatizidwa ndi cholinga chomwe ife timabatizidwira? ______

==========================================================================

10. Yesu sanabatizidwe ndi cholinga monga chathu.

Kodi ndi chiyani chinali chosiyana pa moyo wa Yesu chomwe chinapanga ubatizo wake kukhala wosiyana?

__________________________________

==========================================================================

11. Yesu sanachite tchimo lililonse. Kumeneku ndiko kusiyana kwake. Ife timabatizidwa chifukwa cha tchimo. Yesu sanabatizidwe chifukwa cha tchimo. Kodi ndi chifukwa chiyani Iye anabatizidwa? Funso limeneli ndi lovuta kuliyankha. Buku Lopatulika silitipatsa ife yankho lokwanira koma mawu amene Yesu analankhula kwa Yohane amatithandiza.

Mateyu 3:15:

> Koma Yesu anayankha, nati kwa iye, "Balola tsopano: pakuti kuyenera ife kukwaniritsa chilungamo chonse motero."

Kodi Yesu anaganizira kuti Yohane ayenera kumubatiza Iye? ____________

====================================================================

12. Yesu amadziŵa kuti Yohane anali woyenera kumubatiza Iye. Iye anati, "Balola tsopano." Iye anali kutanthauza kuti, "Loleni kuti ndibatizidwe." Iye ananenanso kuti, "Pakuti kuyenera ife kukwaniritsa chilungamo chonse motero." Zimenezi Iye anatanthauza kuti, m'njira imeneyi ndidzachita chifuniro chonse cha Mulungu." Cholinga cha kukhala wobatizidwa ndi chakuti Iye akhoze kuchita chifuniro cha Mulungu.

Taganizirani za zomwe taphunzira. Kodi Yesu nthaŵi zonse anali kuika ndani kukhala woyamba m'moyo mwake?

____________________

====================================================================

13. Yesu nthaŵi zonse anali kuika Mulungu kukhala woyamba m'moyo wake. Nthaŵi zonse Iye anali kufuna kuchita chifuniro cha Mulungu Atate wake. Mulungu anafuna kuti Mwana wake akhale wobatizidwa. Iye anafuna kuti akhale monga ife.

Ahebri 2:17:

> Potero kudamuyenera kufanizidwa ndi abale m'zonse; kuti akadzakhala mkulu wa ansembe wachifundo ndi wokhulupirika m'zinthu za kwa Mulungu kuti apereke dipo la zoipa za anthu.

Yesu anali monga ife. Iye anali ndi thupi ndi mwazi monga wathu. Iye anali kuvutika monga momwe ife timavutikira. Iye anabatizidwa monga momwe ife timabatizidwira.

Mphunziro ili kodi Yesu anachita chiyani mmalo mofuna kuchita chifuniro cha Mulungu?

____________________

14. Yesu anayenera kubatizidwa. Iye anadzipanga yekha kukhala monga anthu amene anadzaŵapulumutsa. Chinali chifuniro cha Mulungu kuti Yesu achite zimenezi. Choncho Iye anayenera kubatizidwanso mmalo mofuna kuchita chifuniro cha Mulungu.

Kodi Yesu anabatizidwa chifukwa cha tchimo lake? ____________

==============================================================

15. Yesu sanabatizidwe chifukwa cha tchimo. Yesu sanachimwe. Ife timabatizidwa kuonetsa kuti tinatembenuka kusiya machimo athu.

Kodi Yesu anabatizidwa chifukwa chiyani? ____________

______________________________________________________________

==============================================================

16. Yesu anabatizidwa chifukwa chofuna kuchita chifuniro cha Mulungu.

Yesu sanabatizidwe ndi chifukwa monga chathu ayi. Kodi ndi kusiyana kotani kwa ubatizo pakati pa Yesu ndi ife?

____________

______________________________________________________________

==============================================================

17. Kusiyana kwake ndi kwakuti Yesu anali wosachimwa. Iye sanayenera kubatizidwa chifukwa cha tchimo lake ayi.

Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anabatizidwa? ____________

______________________________________________________________

==============================================================

18. Iye anabatizidwa mmalo mofuna kuchita chifuniro cha Mulungu. Yesu anali kufuna kutsata chifuniro cha Mulungu. Iye anafuna kuchita zonse za chifuniro chonse. Yesu anati, Iye anayenera kukhala wobatizi-

dwa mmalo mofuna kucnita zonse zimene zinali zolungama.

Kodi Yesu anali kunena kwa yani kuti Iye ayenera kubatizidwa ndi kukonzekera ntchito yake? ______________________________

==========================================================================

19. Yesu analankhula zimenezi kwa Yohane Mbatizi.

Yesu sanabatizidwe ndi cholinga monga chathu ayi. Kodi n'chiyani chimene chinali chosiyana pa moyo wa Yesu chomwe chidapangitsa ubatizo wake kukhala wosiyana? ______________________________

Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anabatizidwa? ______________________________

______________________________

==========================================================================